

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO
KUPITA KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

KULIMBA MTIMA KWA YOHANE M'BATIZI

(Kulongosola nkhani yomwe yatengedwa kuchokera pa Marko 6:17-28 mwa tsatanetsatane.)

Kuseka kwa chikhakhali kunadzadza nyumba yonse pamene Herode Antipa, bwanankubwa wa dera la ku Galileya, amadyerera ndi kumwerera pamodzi ndi akazembe ake, atsogoleri ake a nkondo ndi akulu ena. Phwandolo linali lokondwerera tsiku lobadwa Herode. Mowa unali wochuluka wochita kusamba pamene anthu amamuchemerera Herodiyo kuti ndi mtsogoleri wamphamvu. Salome, amene anali mwana wamkazi wa Herodiya mkazi wake, anayamba kuvina pamaso pa anthuwo, ndi kuwasangalatsa ndi kukongola komanso chikoka chake.

Chifukwa chakuti kuchemereredwa kunafika m'mutu pa nthawiyo, Herodi anamuyitana namuza kuti; "Tapempha kwa ine chiri chonse uchifuna, ndidzakupatsa iwe. Chiri chonse ukandipempha ndidzakupatsa, kungakhale kukugawira ufumu wanga."

Posinkhasinkha zakuti angapemphe chiyani chabwino, Salome anatuluka nakafunsira nzeru kwa amayi ake. Herodiya anathawa kwa mwamuna wake woyamba, Herode Filipo, nkutengana ndi mchimwene wake wina wa Herode dzina lake Antipa. Iye anaganizira zimenezi pamene amalingalira za pempho la mwanayo. Antipa anabwera kudzacheza kwa mchimwene wake ndipo maso ake anadyerera pa mlamu wakeyo mpaka

chibwenzi chinayamba. Antipayo anamunyengerera Herodiya kuti asiyaneyo ndi mwamuna wake natengane ndi iyeyo. Mkaziyo anavomera kukwatiwa ndi Antipa



"Si kuloledwa kwa inu kukhala naye mkazi wa mbale wanu."

ngati nayeenso atavomera kusiyana ndi mkazi wake. Chifukwa cha chikondi, kuchuka ndi moyo wokonda zosangalatsa, awiriwo anathetsa mabanja awo oyamba nakwatirana.

Mokwiya, Herodiya anaganiza za munthu uja wolungama wotchedwa Yohane M'batizi. Iye anaumiriza mwamuna wake kuti amuponye Yohane m'ndende. Anthu ochuluka amakhudzidwa ndi ulaliki wa Yohane M'batizi chifukwa unali wa chikoka ndipo anthu ambiri amatengeka naye mtima. Ngakhale Herode yemwe ankasangalala kumvera kulalikirira kwake. Munthu uyu amene amadziwika kuti anali mneneri wa Mulungu anamuza Herode komanso anthu onse kuti, "Si kuloledwa kwa inu kukhala naye mkazi wa mbale wanu."

Atadziwa choyenera kuti achite, Herodiya analamulira Salome kuti afulumire ndipo akapemphe mutu wa Yohane M'batizi uli m'mbale. Herode atamva izi anakhumudwa kwambiri koma nanga akanatani popeza anali atalumbira kale. Mwansangansanga analamulira munthu wonyonga anthu kuti apite ku ndende akadule mutu wa Yohane kenaka ndi kuwubweretsa kwa Salome ndi Herodiya.

Yohane M'batizi, amene anali wonenera za kubwera kwa Yesu Khristu, anataya moyo wake chifukwa cha kulimba mtima kwake ponena choona chenicheni, posawerengera kuti anthu akondwera naye kapena ayi. Pamene atsogoleri ena a chipembedzo amasamalitsa kuti asawakhumudwitse olamulira a dziko, Yohane anamvera Mulungu nalalikirira uthenga wabwino mosanyengerera.

(Yapitirira pa tsamba 2)

Mau a Mkonzi
Tsamba 3

Kusanthula Mau a Mulungu
Tsamba 4

Kusudzulana ndi Kukwa-
tiranso

Tsamba 5-8

Mitala ndi yoletsedwa

Nanga Ana titani nawo?
Tsamba 9

Funso & Yankho

Tsamba 10-11

Kodi Mukudziwa?

Mau a pa Nyengo yake

Tsamba 12

ZIMENE BAIBULO Limaphunzitsa za...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;

Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;

Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

Mkulu wina wolembe mbiri ya Ayuda dzina lake Josephus akunena mu buku lake lotchedwa Antiquities kuti: “Herodiya anachita chosutsana ndi malamulo a dziko lathu, ndi kusudzula mwamuna wake pamene iye anali moyo, nakwatiwa ndi Herode (Antipa) amene anali m’chimwene wa mwamuna wake mu azibambo.”

Herode ndi Herodiya analakwira malamulo a Chiyuda kapena a Mose pa milandu ingapo. Kukanakhala kosavuta kuti munthu wa Mulungu uja asalabadire za uchimo wa nthawi imeneyo, koma Mulungu anali atamutuma kuti akakonzeretu njira yodzeramo Ambuye.

Masiku ano dzikoli ndi lodzaza ndi zonyansa komanso mdima wa zinthu zauzimu. Mtundu wa anthu ukukhala mu nyengo ya chisomo ndi choonadi pamene Yesu anabwezeretsa chiyero ndi ungwiro wa ukwati umene uli chijanano cha mpaka imfa pakati pa mwamuna mmodzi ndi mkazi mmodzi. Ukwati wowomerezeka wa Mulungu ndi umene Mulungu anawukhazikitsa modabwitsa, koma zikhalidwe ndi ndale za masiku ano zikusamutsira kutali dongosolo la ukwati limene Mulungu anakonza. “Kusudzulana ndi Kukwatiranso” zikusutsana ndi mfundo za ukwati ndiponso ndi kuphwaya kowonekeratu kwa Malamulo a Mulungu amene apezeka mu Chipangano Chatsopano.

Akhristu ambiri ali mu maukwati a chigololo amene anthu amati bolaniko komanso mipingo yambiri imawavomereza. Choonadi pa mutu uwu chikhoza kukhumudwitsa anthu amene sanalape, komabe chidzamasula ndi kuchenjeza komanso kupereka chilimbikitsa kwa iwo amene ena akuganizira zolowa m’banja. Sitiyenera kukhala chete chifukwa choopa kuti tikhumudwitsa anthu ena.

Kodi a Yohane M’batizi a nthawi ino ali kuti?

-mws

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m’dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata uyu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoonza za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawo amene ali muyeso wowomerezeka wa chikhulupiriro. Amaphunzitsa chipulumutso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudzera mu ntchito ya maombedwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chiyero choonekera pa gawo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wowomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & Rene Smith

KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu iliyonse molingana ndi chitsogozo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa email, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.us. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma email a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choonadi imasindikizidwa mu maiko osiyanasijana kuti igawidwe m’mailkoko. Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zaufulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

The Gospel Truth, 605 Bishops Ct., Nixa, MO 65714 USA

editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Pakuti ndidana nako kuleka kumene, ati Yehova Mulungu wa Israyeli...

—Malaki 2:16

Zinamumvetsa chisoni Mulungu pamene, atawalera ndi kuwasamalira anthu ake osankhika Aisrayele, iwo anamutembenukira nachita tchimo la chigololo ku uzimu potsatira ndi kupembedza milungu ina. Mulungu analenga anthu kuti pakhale mgwirizano ndi umodzi, koma munthu, chifukwa cha uchimo wake, wabweretsa kuwonongeka kwa zinthu komanso ululu. Mulungu amadana ndi kusiyana ukwati komanso kusudzulana, popeza amadziwa bwino zotsatira za mchitidwewu.

Mtolo umene ndafuna kuti ndigawane nanu ulendo uno uli pa mutu wakuti Kusudzulana ndi Kukwatiranso. Pokhapokha ngati tikuwonjezerapo zina, koma tikanena kuti “Kusudzulana ndi Kukwatiranso” mu kalatayi tikuntanthauza chinthu chimodzi. Monga mmene ndimachitira ndi mitu yambiri, sindingakwanitse m’kalata yaying’ onoyi kulemba zonse zomwe zili pa mutuwo komanso sindingathe kulongosola bwino lomwe zina zimene malemba amanena ndi chilichonse chokhudza nkhanayi. Pempho langa ndilo lakuti Ambuye adalitse aliyense wowerenga kalatayi ndi kumupatsa kumvetsetsa koyenera kwa chiphunzitsochi chimene chili chofunikira m’dziko lathuli m’masiku ano.

Kusudzulana ndi kukwatiranso kukuchitika kwambiri osati pakati pa anthu osapembedza okha, komanso ngakhale pakati pa akhristu olimba. Yesu anaphunzitsa momveka bwino kuti kusudzulana ndi kukwatiranso kuli kunja kwa chifuniro cha Mulungu. Anthu atembenuza malemba navesayesa kuti apeze danga lololeza kuti ukwati ukhoza kuchitika pamene winayo akadali moyo. Ndinamva Mbusa wina wa mpingo wa Church of God penapake akuchitira umboni pamene anasiya mkazi wake. Iye anati, “Ambuye anandiuza kuti sindiyenera kukhala osakwatira.” Komatu zoonza zake ndizo zakuti Mzimba Woyera sadzatitsogolera ku chinthu chimene chili chotsutsana ndi Mau a Mulungu.

Kusudzulana ndi Kukwatiranso ndi chinthu chimene chikuwononga mabanja ambiri. Ana akuzunzika chifukwa cha kudzikonda ndi uchimo wa makolo awo. Mulungu anakonzika kuti mwana adzikulira mu banja limene bambo ndi mayi akukhalira limodzi. Anthu amafuna njira yachidule m’dziko lathu lino. Ngati chinthu chili chofunikira, zimafunika mphamvu komanso kuyikirapo mtima kuti chisatayike. Palibe chimene chingalowe m’malo mwa banja loopa Mulungu ndi lokhutira, koma zimatengera kudzipereka kwathunthu. Kukwatiranso si yankho la banja limene likudutsa m’mavuto. Imeneyi ndiyo nthawi yakuti mufunefune nkhope ya Mulungu ndikupempha kwa lye chisomo, chikondi ndi chikhululukiro chochuluka.

Tonsefe miyoyo yathu yakhudzikapo ndi kusudzulana komanso kukwatiranso. Nkoyenera kuti tisalozerele kufala kwake kwa mchitidwewu kuti kutiletse ife kulengeza za chifuniro chonse cha Mulungu. Monga tanenera kale, kungokhala chete osayankhulapo kumapangitsa kuti anthu atayirire.

Ndikufuna ndipemphe kholo lililonse, mphunzitsi aliyense wa Sande sukulu, ndi mbusa aliyense kuti aphunzitse ana ndi achinyamata zoonadi zenizeni za nkhanayi. Ukwati ndi mpaka imfa ndipo sitingangowutayira kuchire ngati chinthu chopanda ntchito. Satana amafuna kuti zinthuzi zioneke chonchi. Koma Mulungu ali ndi pulani yabwino yokhudza ukwati. Tiyeni titsatire njira ya Mulungu!

Michael W. Smith

October 2015

Zambiri Zili pa

INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira

makalata athu kapenanso

kuti muone. makalata

akale.



Zofunikira kuti mukhale ndi Banja losangalala

*Chikondi
Kumvera
Kupereka
Kulemekezana
Kukhululukira
Kuvomera
Kudzikhuthula
Kupemphera
Kulimbikitsana
Kukhulupirirana
Kusungirana
ulemu
Kuthandizana*

KUSANTHULA MAU A MULUNGU

MUTU: KUSUDZULANA NDI KUKWATIRANSO

Malemba: Yense wokusudzula mkazi wache, nakwatira wina, achita chigololo; ndipo iye amene akwatira wosudzulidwayo, achita chigololo. —Luka 16:18

Mau mwa chidule:

Ukwati, kuyambira pachiyambi, unali chiyanjano cha mpaka imfa pakati pa mwamuna mmodzi ndi mkazi mmodzi. Chiyanjano chimenechi chinadetsedwa ndi mitala komanso kusudzulana ndi kukwatiranso. Yesu anabwezeretsa chiyero cha ukwati. Kukwatiranso pamene mkazi kapena mwamuna woyambayo ali moyo ndi chigololo ndithu.

I. Pachiyambi

- A. Genesis 2:18 Mulungu anamulengera Adamu munthu womuthangatira.
- B. Genesis 2:23-25 Chiyanjano cha mwamuna mmodzi ndi mkazi mmodzi.

II. Ukwati wa amuna kapena akazi okhaokha ndi oletsedwa

- A. Levitiko 20:13 Ndi chonyansa.
- B. Aroma 1:26-32 Maganizo opotoka.
- C. I Akorinto 6:9 Sadzalowa mu ufumu wa Mulungu.

III. Lamulo la Mose

- A. Eksodo 20:14 Mulungu amaletsa chigololo.
- B. Deuteronomo 22:22-29 Chilango cha chigololo ndicho imfa.
- C. Deuteronomo 24:1-4 Mose analolera kusudzulana.
- D. Marko 10:2-5 Chifukwa cha kuuma mtima kwawo.

IV. Lamulo la Khristu

- A. Marko 10:2-12
 - 1. Vss. 6-7 Ukwati uli pakati pa mwamuna ndi mkazi; Kusudzulana ndi koletsedwa kuyambira pachiyambi.
 - 2. Vss. 8-9 Chiyanjano cha ukwati chisaduke.

3. Vss. 10-12 Kusudzula ndi kukwatiranso ndi chigololo ndithu.

B. Luka 16:18 Iye amene akwatira munthu wosudzulidwa achita chigololo.

C. Mateyu 5:31-32 Gwero la tchimo la chigololo.

V. Zomuyenereza munthu kuti

Akwatiwenso kapena Kukwatiranso

- A. Aroma 7:1-3 Imfa imamwasula munthu ku ukwati. Kukwatiranso ndi tchimo kupatula kwa akazi kapena amuna amasiye.
- B. I Akorinto 7:10-11 Ngati mwasiyana, musakwatirenso kapena kukwatiwanso.
- C. I Akorinto 7:39 Imfa imamasula; kwatiwani mwa Ambuye.

VI. Chiweruzo cha Chigololo

- A. Ahebri 13:4 Mulungu adzaweruza.
- B. Agalatiya 5:19-21 Ntchito za thupi.
- C. I Akorinto 6:9 Sadzalowa ku ufumu wa Mulungu.
- D. Chivumbulutso 21:8 Ali ndi gawo lawo mu nyanja ya moto.
- E. Yohane 8:3-11 Pitani koma musakachimwenso.

Kumaliza:

Ukwati uchitidwe ulemu ndi onse, ndi pogona pakhale posadetsedwa; pakuti adama ndi achigololo adzawaweruza Mulungu.

—Ahebri 13:4

Kusudzulana ndi Kukwatiranso

Pachiyambi pa nthawi,

Mulungu analenga mwamuna. Iye anaona kuti sikwabwino kuti mwamunayo akhale yekha, choncho analenga mkazi kuti akhale womthangatira (Genesis 2:18). Pakutero anayambitsa ukwati. Ukwati unalengedwa ndipo ndi wochokera kwa Mulungu. “Chifukwa chotero mwamuna adzasiya atate wache ndi amache nadzadziphatika kwa mkazi wache: ndipo adzakhala thupi limodzi” (Genesis. 2:24).

Chiyanjano cha ukwati ndi chinthu chachikulu chimene chimawalumizikitsa anthu pamodzi mwa mwa maubale amene alipo pa dzikoli ndipo umangocheperako pang’ono pa ubale umene ulipo pakati pa Mulungu ndi munthu. Ukwati unakhazikitsidwa ndi Namalenga, ndipo cholinga chake chinali chakuti ukhale chiyanjano chimene mwamuna ndi mkazi adzipereka kwa wina ndi mnzake mpaka imfa. Kukwanitsidwa kwa zikhumbokhumbo za thupi ndi mphatso imene imayenera kupezeka mu banja osatinso kwina. Mdierekezi wayesetsa kulimbana ndi chiyero cha ukwati ndipo wachita zonse zotheka kuti awononge mabanja. Dzikoli nalo lapotoza, lasulutsa ndi kupereka tanthauzo lakelake pa nkhani yokhudza ukwati. Palibe kusintha kulikonse kumene kungachitike komwe kungasinthe choonadi cha Mulungu pa nkhaniyi.

UKWATI — MWAMUNA MMODZI, MKAZI MMODZI

Ukwati umene Mulungu amavomereza ndi wa pakati pa mwamuna ndi mkazi. Ukwati wa amuna kapena akazi okhaokha ndiwo kupotoza zoonza zenizeni za ukwati komanso ndi chonyansa pamaso pa Mulungu. Mau a Mulungu amaletsa kukwatirana akazi kapena amuna okhaokha (Levitiko 20:13, Aroma 1:26-32) ndipo amanena kuti aliyense wochita zimenezi sadzalowa mu ufumu wa Mulungu (1 Akorinto 6:9).

MALAMULO A MOSE


Malingana ndi Malamulo a Mose, mkazi amene wangokwatiwa kumene akapezeka kuti sanali namwali, mkaziyo amayenera kuphedwa pogendedwa miyala. Koma ngati amanamiziridwa ndi mwamuna wake, mwamunayo amayenera kumuvomera ndi kumutenga ngati mkazi wake ndipo “sakhoza kumchotsa masiku ache onse.” (Deuteronomo 22:19). Ngati anthu awiri amene sali pabanja agwirizana kuchita chigololo, mwamunayo amayenera kumukwatira mkaziyo ndipo sakanatha kumchotsa (Deuteronomo 22:29).

Malamulo a Mose amanenetsa mwachimvekere kuti: “Usachite chigololo” (Eksodo 20:14). Ngati mwamuna kapena mkazi wokwatira agwidwa akuchita tchimo la chigololo ndi munthu wina, chilango chake chinali kuphedwa pogendedwa miyala (kapena kupotoledwa pakhosi), popeza Mulungu samafuna kuti pakati pa Aisrayele pakhale uchimo (Deuteronomo 22:22-29). Munthu amene anali wosachimwa anali womasuka kukwatiranso chifukwa mwamuna kapena mkazi wake wamwalira.

UKUSUZULA KUMALOLEDWA PANTHAWI YA MOSE

“Patapita nthawi, potengera chitsanzo cha anthu amitundu, tanthauzo la ukwati linasuluka ndipo kaganizidwe ka anthu pa za chigolo kanasintha, ndipo chilango cha imfa chimaperekedwa patalipatali kapena osaperekedwa nkomwe” (*Smith’s Bible Dictionary, Adultery*). Chifukwa cha ichi, kusudzulana ndi kukwatiranso kunachuluka. Mose analoleza kuti kusudzula kukhoza kuchitika pa Deuteronomo

(Yapitirira pa tsamba 6)



—Patrice Doolittle

(Kuchokera pa tsamba 5)

Onse amene akwatira kawiri
potsata chilamulo cha anthu,
ali ochimwa pamaso pa
Mbuye wathu.
– Justin Martyr, 160 AD

24:1-2 pamene akunena kuti: “Munthu akatenga mkazi akhale wache, kudzali, ngati sapeza ufulu pamaso pache, popeza anapeza mwa iye kanthu kosayenera, amlembere kalata wa chilekanitso, ndi kumpereka uyu m’dzanja lache, ndi kumtututsa m’nyumba mwache. Ndipo ataturuka m’nyumba mwache, amuke nakhale mkazi wa mwamuna wina.”

KUSUTSANA KUMENE KUNALIPO PA LAMULO LA CHIYUDA

Malamulo a Mulungu amanenetsa momveka bwino kuti anthu amene apezeka akuchita chigololo ayenera kuti aphedwe, koma kenaka Mose anapereka lamulo lakuti munthu akhoza kulemba kalata yosudzula mkazi wake ngati pali chidetso. Mu nthawi ya Yesu, panali kusutsana kwakukulu pakati pa akatswiri a malamulo a Chiyuda pa za tanthauzo la mau akuti “kudetsedwa” kumene kukhoza kupangitsa kuti munthu asudzule mkazi wake. Ayuda ambiri samalabadira nkomwe za tanthauzo la lamulo limeneli la kusudzulana. Ena mwa aphunzitsi a Malamulo amapereka kalata ya chisudzulo pamene mwamuna kapena mkazi wachita chigololo. Ena amapeputsako malamulowo ndipo amapereka chisudzulo kwa mwamuna ngati waona kuti mkazi wake “alibe nayenso chidwi”. Mwamuna amatha kutenga kalata yomulola kusudzula mkazi wake ngati mkaziyo wapsereza zakudya kapena ali wauve.

LAMULO LA KHRISTU

Afarisi anabwera kwa Khristu kufuna kumutapa mkamwa ndi nkhani yakuti “ngati kuloledwa kuti munthu achotse mkazi wache” (Marko 10:2). Iwo amafunsa za Malamulo a Mose, koma zimene Khristu anayamba kuphunzitsa zinabwezeretsanso kulemerera kwa ukwati monga mmene zinaliri pa nthawi imene dziko limalengedwa. Chiphunzitso cha Khristu chinakweza muyezo wa ukwati ndipo ndicho chiphunzitso chimene timayenera kutsatira lero.

Yesu anawafunsa zimene malamulo a Mose amanena ndipo iwo anayankha kuti; “Mose analola kulemba kalata wakulekanira, ndi kumchotsa” (10:3-4). Yesu anawauza kuti izi zinali choncho “Chifukwa cha kuuma kwa mitima yanu anakulemberani lamulo ili” (10:5). “Koma kuyambira pa chiyambi cha malengedwe anawapanga mwamuna ndi mkazi....ndipo awiriwa adzakhala thupi limodzi: kotero kuti salinso awiri, koma thupi limodzi. Chifukwa chache chimene Mulungu anachimanga pamodzi, asachilekanitse munthu, Kuyambira pachiyambi, kunali kosalolekwa kusudzulana, koma zinachitika chifukwa cha kuuma mitima ndi kuchimwa kwa anthu kumene kunapangitsa Mose kuti alole za kusudzulana. Pamenepa Yesu anaphunzitsa kuti ukwati ndi chiyanjano chimene sichiyenera kudulidwa ndi munthu. Pamaso pa Mulungu, palibe lamulo la dziko kapena la chipembezidzo limene likuyenera kuposa chiyanjano cha ukwati. Iye anawakaniza Afarisi aja ufulu umene amafuna kuti akhale nawo kuti potero akhoza kuchita chilichonse chimene iwo akufuna motsatira lamulo la Mose lija.

“Mwamuna amatha
Kutenga chilolezo
chosudzula
mkazi wake ngati
wapsereza chakudya
kapena zakonza
mnyumba”

[Miyambo yochitika pakati pa Ayuda]

MAYANJANO A MCHIGOLOLO

Ophunzira a Khristu amavutika ndi nkhanayi monga mmene anthu ambiri amachitiranso lero. Iwo anamufunsa Yesu kangapo za nkhanayi, choncho Yesu analankhula momveka bwino kuti, “Munthu ali yense akachotsa mkazi wache, nakakwatira wina, achita chigololo kulakwira mkaziyo; ndipo ngati mkazi akachotsa mwamuna wache, nakwatiwa ndi wina, achita chigololo iyeyu”

(Marko 10:10-12). Malemba amenewa anali omveka bwino ndithu. Yesu ananena mosazungulira kuti ngati munthu asiya mkazi wake nakwatira wina, iyeyo akuchita chigololo. Izi zili choncho

chifukwa mkazi watsopanoyo sangakhale mkazi wake weniweni ndipo ukwatiwu udzakhala wa chigololo.

**“Ukwati ndi
mpaka muyaya ndipo
pamaso pa Mulungu
ndipo ukhalabe
chomwecho, ngakhale
munthu achite zimene
akuganiza kapena
akhale ndi mayanjano
ena.”**

Yesu anapitiriza kuphunzitsa pa Luka 16:18: “Yense wakusudzula mkazi wache, nakwatira wina, achita chigololo; ndipo iye amene akwatira wosudzulidwayo, achita chigololo.” Si mwamuna yekha amene achita tchimo la chigololo pamene akwatiranso komatu ngakhale mkazi wake wosudzulidwayo, ali wosalakwa choncho, akakakwatiwa nayenso achita chigololo. Ambuye safuna kuti anthu akasudzulana adzikwatiranso pofuna kupereka kwa onse awiri mwayi wakuti akhoza kuyanjananso ndi kubwererana.

Ukwati ndi mpaka imfa ndipo uli choncho pamaso pa Mulungu, ndipo izi sizitengera mmene anthu amaonera kapena kuganizira. Yesu anabwezeretsa lamulo la ukwati – lamulo lake limene Iye anapereka pachiyambi.

POKHAPOKHA NGATI WINA WACHITA CHIGOLOLO

“Kunanenedwanso, Yense wakuchotsa mkazi wache ampatse iye chilekaniro: koma Ine ndinena kwa inu, kuti yense wakuchotsa mkazi wache, kosati chifukwa cha chigololo, amchititsa chigololo: ndipo amene adzakwata wochotsedwayo achita chigololo” (Mateyu 5:31-32). Malingana ndi mbiri ya Chiyuda, kalata ya chikelaniriro imanena kuti munthu wosudzulidwayo ali ndi ufulu akuti akhoza kukwatiwanso. Chimenechi ndiye chifukwa chomwe Yesu ananena kuti “amchititsa chigololo.” Ngati iye sanachite china chilichonse cholakwika, mwamunayo ndiye wamupangitsa kuti achimwe ngati mkaziyo akwatiwanso. Ngati mwamuna asudzula mkazi wake chifukwa cha tchimo la chigololo, analibe mlandu pamaso pa Mulungu popeza mkaziyo anali wachigololo. Yesu sanadzudzule za “kusudzula” chifukwa cha chigololo. Iye sanapereke mpata wakuti zinthu zikatero munthu akhoza kukwatira kapena kukwatiwanso.


IMFA YOKHA IMALEKANITSA CHIYANJANO CHA UKWATI

Mtumwi Paulo naye analongosolapo za nkhanu ya ukwati. Ndi imfa yokha imene imamumasula munthu wapabanja kuti asakwatiwanso. “Pakuti mkazi wokwatidwa amangidwa ndi lamulo kwa mwamuna wache wamoyo; koma mwamunayo akafa, iye amasulidwa ku lamulo la mwamunayo. Ndipo chifukwa chache, ngati iye akwatiwa ndi mwamuna wina, pokhala mwamuna wache wamoyo, adzanenedwa mkazi wachigololo; koma mwamunayo akafa, iye amasulidwa ku lamuloli; chotero sakhala wachigololo ngati akwatiwa ndi mwamuna wina” (Aroma 7:2-3). Apa akutsimikiza kuti ngati munthu wina akwatiranso pamene mnzake wa banja ali moyo, iye akukhala mu chigololo.

NGATI MWASIYIDWA UKWATI, MUKHALEBE OSAKWATIRA KAPENA OSAKWATIWA

Pali nyengo zomvetisa chisoni ndi zosautsa pamene abambo kapena amayi apezeka kuli ali okha chifukwa mnzawo wa banja anawathawa nakalowa ku banja ndi munthu wina umene uli moyo wauchimo ndithu komanso wachigololo. “Koma okwatitsidwawo ndiwalamulira, si ine ai, koma Ambuye, kuti mkazi asasiye mwamuna, komanso ngati amsiya akhale osakwatiwa, kapena ayanjanitsidwanso ndi mwamunayo, ndipo mwamuna asalekane naye mkazi” (1 Akorinto

(Yapitirira pa tsamba 8)



Ukwati ndi chisankho cha mpaka imfa...Nkofunikira kuti iwo amene ali aang'ono komanso akulu onse aganizire za ukwati mopemphera bwino komanso mosamalitsa.

7:10-11). Ngati zinthu zafika povuta ndipo iwo awiri sakugwirizana mpaka asiyana, iwo akhalebe choncho osakwatira kapena kukwatiwa ngati onse ali moyo. Mulungu wathu, kudzera mu mphamvu ya Yesu Khristu, amapereka chisomo chapaderadera ndi kuthereka komuthandiza munthu wotere kuti akhoza kukhala yekha komanso kuti asunge chiyeero.

MABANJA A ANTHU AMENE SANAPULUMUTSIDWE

Paulo akupitiriza kupereka malangizo a mmene munthu angakhaliye m'banja ndi mnzake amene ali wosapulumsidwa—ngati wosapulumsidwayo akufunabe kupitiriza kukhala mu ukwatiwo—kuti asamusiye ukwati. Mwachidziwikire, ngati munthu ali mu moyo wa chigololo, ichi chikhoza kukhala chizindikiro kuti iye “sakusangalatsidwa kukhala pamodzi” ndi mkazi wakeyo. “Koma ngati wosakhulupirayo achoka, achoke. M'mirandu yotere samangidwa ukapolo mbaleyo, kapena mlongoyo. Koma Mulungu watiitana ife mumtendere” (1 Akorinto 7:12-15). Wokhulupirirayo akadali womangidwa mu ukwatiwo, koma osati ku ubale wake ndi Mulungu ndipo sali kapolo kapena wolakwa chifukwa cha zochita za mnzake uja (Onani pa Mateyu 5:31-32). Mwanjira ina iliyonse, zimenezi sikuti zikumumasula munthu wosalakwa uja kuti akwatiwenso. Paulo akumaliza ndimeyi pakubwerezanso kuti: “Mkazi amangika pokhala mwamuna wache ali ndi moyo; koma atamwalira mwamuna ali womasuka, kuti akwatiwe naye amene afuna, koma mwa Ambuye” (1 Akorinto 7:39).

MUSAKWATIRE WOSAKHULUPIRIRA

Nkofunikira kuzindikira kuti ngati ukwatiwo uli woyamba kapena wachiwiri (koma wovomerezeka), anthu akwatirane opulumuka okhaokha. “Mukwatire mwa Ambuye.” Ambiri ataya chipulumutso chawo pokwatira munthu wina amene ali kunja kwa chikhulupiriro. Mwana wa Mulungu, samalani, musalole kuti zikhumbokhumbo zanu zipite kwa munthu amene ndi wosapulumsidwa.

CHIYEMBEKEZO KWA IYE AMENE ALI WACHIGOLOLO

“Ukwati uchitidwe ulemu ndi onse, ndi pogona pakhale posadetsedwa; pakuti adama ndi achigololo adzawaweruza Mulungu.” (Ahebri 13:4). Chigololo ndi ntchito za thupi ndipo “iwo akuchitachita zotere sadzalowa Ufumu wa Mulungu” (Agalatiya 5:19-21).

Yesu anafera iwo amene ali mu chigololo, ndipo pali chifundo ndi chikukhululukiro (Yohane 8:3-11). Ambuye amakonda munthu wachigololoyo koma amafuna kuti iye aleke mayanjano ake achigololo. Ngakhale pali zotsatira zake za tchimoli, Mzimu Woyera akhoza kubweretsa moyo umene uli wolapawo ndi kuwufikitsanso pamaso pa Mulungu.

Mu Chipangano Chatsopano, Malemba akutiphunzitsa momveka bwino kuti ukwati sukuyenera kutha. Kusudzulana ndi Kukwatiranso sizili mu dongosolo la Mulungu yokhudza nkhanu ya ukwati. Ukwati ndi chisankho chimene munthu ayenera kuchipanga mpaka imfa, ndipo chifukwa cha ichi, nkofunikira kuti onse, achinyamata ndi akulu omwe aganizire mozama za ukwati mopemphera komanso mosamalitsa—popeza pamakhala mwayi umodzi basi. Ukwati ndi wolemekeza ndipo ndi mdalitso pamene dongosolo la Mulungu likutsatidwa.

—mws

Mitala ndi Yoletsedwa

Chinali chikhalidwe ndithu pakati pa amuna ambiri a mu Chipangano Chakale kukwatira mkazi oposa mmodzi (mitala), koma mmene Mulungu adaakonzero kuyambira pachiyambi kunali kuti mkazi mmodzi adzikhala wa mwamuna mmodzi, chimodzimodzinso mwamuna. Mu Chipangano Chatsopano, Khristu anabwezeretsa cholinga chenicheni cha ukwati.

“Kodi simunawerenga kuti Iye amene adalenga anthu pachiyambi, anawalenga iwo mwamuna ndi mkazi, nati, Chifukwa cha ichi mwamuna adzasiya atate wache ndi amache, nadzaphatikizana ndi mkazi wache, ndipo awiriwo adzakhala thupi limodzi? Chotero kuti salinso awiri koma thupi limodzi” (Mateyu 19:4-6).

“Awiriwo” sakutanthauza atatu kapena anayi. Akunena momveka bwino ndithu kuti awiri. Mulungu analenga mkazi mmodzi, Hava, kuti akhale wa Adamu. Sanamulengerenso Adamuyo mkazi wina wotchedwa Marita kuti potero banja likhale lokwanira. Ngakhale mitala imachitika m’maiko ambiri masiku ano, chimenechi chikutsutsana ndi dongosolo la Mulungu. Ndi mau ochepa chabe, Khristu anadzudzula mchitidwewu ndiponso anabwezeretsa chiyanjano chabwino mntawu ino ya chisomo chimene anachikonzeratu kuyambira pa nthawi yakulengedwa kwa dziko lapansi.

Paulo, pamene akupereka malangizo kwa Timoteo, ananena kuti, “woyang’anira akhale wopanda chirema, mwamuna wa mkazi mmodzi...” (1 Timoteo 3:2). Paulo samanena kuti munthu akhale wokwatira basi, koma amadzudzula mitala. Munthu amene ali ndi akazi oposa mmodzi, samaloledwa kukhala mkulu woyang’anira mpingo, popeza iye amayenera kukhala chitsanzo cha dongosolo labwino la Mulungu pa ukwati. ❖

Nanga Ana titani nawo?

Pamene bambo kapena mayi wasudzula mnzake wa banja nkukakwatiranso, iyeyo wachita chigololo. Izi ndi zoonanso kwa anthu amene ali pa ukwati wa mitala. Iyi ndi nzeru ya mdierakezi pofuna kuwayika mu msampha anthu amene ali mu maukwati oterewa kuti pakutero asathe kupulumuka. Pamene anthu apulumuka, iwo amasiya uchimo nayamba kukhala m’moyo wachiyero. Maukwati amene ali a chipwirikiti amabweretsa chisokonezo komanso amapweteketsa mtima. Zilipo nyengo zina pamene nkovuta kumasula zimene zinamangika kale, koma alipo Mpulumutsi amene amapereka nzeru ndi kuthereka kuti muturuke mu mavuto amenewa. Mzimu Woyera adzakutsogolerani ku choonadi chonse ndipo sadzatsogolera mosemphana ndi Mau a Mulungu.

Nthawi zambiri ana amabadwa mu ukwati wa chigololo kapena wa mitala. Ana amenewa ndi osachimwa pamaso pa Mulungu ndipo alibe mlandu wa cholakwa chilichonse. Pamene munthu wapereka mtima wake kwa Mulungu, nakhala molingana ndi choonadi cha Mau a Mulungu, iye adzafunitsitsanso kuti ukwati wake ukhale molingana ndi dongosolo la Mulungu. Pamene tiyenera kuleka tchimo, izi sizitanthauza kuti munthu asasamalire ana ake – ngakhale iwo amene abadwa ku ukwati wachigololo kapena wamitala.

Paulo ananena kuti, “Koma ngati wina sadzisungiratu mbumba yache ya iye yekha, makamaka iwo a m’banja lache, wakana chikhulupiriro iye, ndipo aipa koposa wosakhulupira” (1 Timoteo 5:8). Bambo ali ndi udindo woonetsetsa kuti ana ake, kaya akuchokera ku ukwati wotani, akusamaliridwa m’magawo onse mpaka adzakule. Iwo alipo chifukwa cha tchimo la bamboyo, ndipo nkoyenera ndithu kuti bamboyo adziwonetsetse yekha monga wokhulupirira pokuwasamalira ndi kuwayang’anira.

Chimakhala chinthu chomvetsa chisoni pamene bambo afika kunyumba nayamba kumenya mkazi wake wachiwiri komanso ana ake a maiyo nkuwapirikitsira kumsewu kuti akakhale amasikini, nkumalengeza kuti akuchita izi chifukwa tsopano iye ndi munthu wa Mulungu. Iyetu akadali ndi udindo kwa ana ake aja pokhala kuti iye ndi tate wao. Chimodzimodzinso, pamene sangakhalirensa limodzi ndi mkazi amene sali wovomerezeka, iyeyo akadali ndi udindo woonetsetsa kuti maiyo akusamaliridwa bwino lomwe mwa umulungu. Chimakhala chinthu chanzeru kuti anthu amene apezeka mu vuto ngati ili, afunsire uphungu woyenera kwa anthu a Mulungu. ❖



*Koma ngati wina sadzisungiratu
mbumba yache ya iye yekha,
makamaka iwo a m’banja lache,
wakana chikhulupiriro iye,
ndipo aipa koposa wosakhulupira.
(1 Timoteo 5:8).*



“Lamulo lovomerezeka
Potanthauzira
Malemba limadziwika
kuti
‘Kugwirizana kwa
Chikhulupiriro.’
Mau a Mulungu
Sadzitsutsa okha.”



Funso: Kodi mungathe kufotokozera ndime ya pa Mateyu 19:9 imene ena amagwiritsa ntchito pofuna kukwatiranso mnzawo wa banja atachita chigololo?

Yankho: Kukadakhala kovuta kulemba pa mutu wa Kusudzulana ndi Kukwatiranso osafotokozera ndime imene ikupezeka pa Mateyu 19:9 pamene akunena kuti: “Ndipo lne ndinena kwa inu, Amene ali yense akachotsa mkazi wache, kosakhala chifukwa cha chigololo, nadzakwatira wina, achita chigololo: ndipo iye amene akwatira wochotsedwayo, achita chigololo.”

Lamulo limene limagwiritsidwa ntchito potanthauzira ndime imeneyi limatchedwa kuti “Kugwirizana kwa Chikhulupiriro.” Izi zikutanthauza kuti pali mgwirizano komanso kulumikizana pamodzi kwa Malemba osiyanasiyana ndipo sasutsana. Malemba amene ali ovuta kuwamvetsa nthawi zonse amakhala ndi mau enanso pena amene ndi osavuta kuwamvetsa. Chifukwa cha ichi, chiphunzitso chisamakhazikike pa ndime imodzi yokha koma ndime zingapo m’malemba zidzigwirizana. Mau a Mulungu sadzitsutsa okha.

Malemba anenetsa mwachimvekere kuti ukwati ndi mpakana imfa. Ngakhale anthu atasiyana chifukwa chakuti winayo samakhulupirika m’banjamo, ukwati umene ungachitike mwa njira ina iliyonse pamene winayo akadali moyo umatengedwa ngati chigololo pamaso pa Mulungu. Ndime zimene zikupezeka ku Mateyu 5:32, Luka 16:18, Marko 10:11-12, ndi 1 Akorinto 7:10-11, 39 zonse zikunena momveka bwino za nkhanayi. Choncho, ndime ya pa Mateyu 19:9 iwunikiridwe molingana ndi maziko amenewo.

Ndime yotsatirayi yachokera pa zolembe za Mbale Ostis Wilson zokhudza nkhanayi:

Kumvetsetsa kwanga kwa nkhanayi ndi kwakuti ili ndi magawo awiri. Afarisi adamufunsa Yesu ngati kunali koyenera kuti munthu asudzule mkazi wake pa chifukwa chilichonse (vesi 3). Funso lawo lalikulu linali limeneli. Iwo sanafunse za kukwatiranso munthu atasudzula mkazi wake. Imeneyo sinali nkhani kwa iwo iwo chifukwa pakati pawo zoterezi zimachitika ndithu, ndipo kusudzulana ndi kukwatiranso kunali kololedwa mwa lamulo. Ena mwa iwo anali ndi akazi angapo amene amakhala nawo limodzi imene inali mitala.

Mu gawo loyamba la ndime imeneyi, Yesu anayankha funso lawo nalongosola bwino za cholinga chenicheni ndiponso dongosolo la Mulungu pa ukwati kuti chifukwa chokwanira chimene munthu akhoza kusudzula mkazi wake ndi pamene wachita chigololo. Izi zikufanana ndi nkhani ya ku Mateyu 5:32 pamene akunena zomwezo ndiponso kutsimikiza kuti munthu ali ndi ufulu kusudzula mkazi wake kapena mwamuna wake chifukwa cha chimechechi, popeza pali maumboni awiri, ndipo molingana ndi Mau a Mulungu, mau aliwonse amakhazikitsidwa pamene pali mboni ziwiri (Mateyu 18:16 ndi Yohane 8:17). Kufikira pamenepa, nkhani ya “Kusiya mkazi” ikuganiziridwabe. Kenaka, atawayankha funso lawo lija, Yesu anapitiriza kuyankhula nabweretsa chiphunzitso chake cha mu Chipangano Chatsopano – chakuti ngati munthu wina akwatira mkazi amene wina wamusiya, nayenso achita chigololo. Nzosadabwitsa kuti zimenezi zinawadzidzimutsa

Afarisi aja ndipo zikuwonekeranso kuti nawo akuphunzira anadabwa nazo chifukwa cha yankho limene anapereka lakuti: “Ngati mlandu wa munthu ndi mkazi wache uli wotere, sikuli kwabwino kukwatira.” (Mateyu 19:10). Zikuonekeratu kuti anthu awa osankhikawa anamvetsetsa kuchokera ku zimene Yesu anayankhula kuti ukwati suyenera kutha chisawawa ndipo ngati zili choncho kuti nkovuta kutulukamo, kungakhale kwabwino osalowamo.

Chifukwa cha ichi, molingana ndi mau a Mateyu 19:9, ndimaliza ndi kunena kuti munthu akhoza kusiya mkazi wake pachifukwa chokha cha chigololo ndipo palibenso chifukwa china, ndipo zikatero ngati iye akwatira mkazi wina wosiyidwayo akadali moyo, pamenepo naye achita chigololo. Pa Mateyu 5:32 Yesu akunena motsindika pa nkhanayi ndipo akuti ngati munthu asiya mkazi wake pachifukwa china osakhala chigololo, amupangitsa mkaziyo kuchita chigololo. Mwa njira ina tinganene kuti, iye ndi amene wachititsa kuti mkaziyo alowerere mmoyo wachitayiko pomusiya pamene anali mkazi womvera ndi wokhulupirika. Mulungu adzamufunsa mlandu wa mkaziyo chifukwa chomupangitsa kuti achite zolakwikazi komanso pomuyika pamalo akuti akhoza kuyesedwa.

Mau akuti “chigololo” mu chilankhulo cha Chigriki ndi *porneia*, ndipo amatanthauza uhule kapena chisembwere. Tanthauzo lake ndi limakhudza madera ambiri kusiyana ndi mmene timachitira lero pamene timangoganiza za kugonana kwa anthu awiri amene si banja. Mau akuti *Porneia* amatanthauza tchimo lililonse lokhudzana ndi chiwerewere pamene chigololo chikunena za munthu wapabanja amene agona ndi wina amene sali mwamuna wake kapena mkazi wake.

Pa Mateyu 5:32 komanso Mateyu 19:9 akutionetsa kuti pakhoza kukhala chifukwa chakuti anthu asiyanen ngati tchimo la chigololo lapezekapo, komabe sakupereka chilolezo chakuti munthu akwatirensa. Yesu anati “ndipo amene adzakwata wochotsedwayo achita chigololo.” Iye sanasiyanitse pakati pa mkazi wosiyidwa chifukwa chakuti wachita chigolo ndi mkazi wosiyidwa chifukwa cha zifukwa zina. Ngati kukwatiranso kunali kololedwa, iye akanasiyanitsa pamenepa. Malemba onse a ku Chipangano Chakale akukhazikika pa mfundo yakuti ukwati ndi mpaka imfa, ndipo izi sizitengera machimo a mmodzi wa awiriwo m’banjamo.

Wolemba wina dzina lake Matthew Henry, ananena motere pa nkhanayi:

Ukwati ndi chinthu chimene sichiyenera kupasuka mwachisawawa ndipo izi sizitengera zofuna kapena ntchito za anthu koma pa mfundo zimene zinakhazikitsidwa pa chiyambi. Khristu, pamene anakonzanso malamulo a Mose amene anali atakhwefulako zinthu zina komanso ndi kubwezeretsa ukwati ku cholinga chake chenicheni, iye analimbikitsa lamulo lolemekezeka la ukwati, kuti akuletsa zinthu zosiyanasiyana zimene anthu akhoza kuchita pofuna kulimbikitsa uchimo, monga kugwirizana kwa mwamuna ndi mkazi ndi cholinga chongofuna kuti apeze mwayi wokwatira ndi anthu ena.

Mamasulire a Chipangano Chatsopano a *Emphatic Diaglott*, amene kwambiri atengera mamasulire a *The Vatican Manuscript*, amalemba motere: “Ndipo Ine ndinena kwa inu, aliyense amene adzachotsa mkazi wache, pokhapokha ngati sichili chifukwa cha chigololo, achititsa mkaziyo kuti achite chigololo; ndipo iye amene akwatira wochotsedwayo, achita chigololo” (Mateyu 19:9).

Nkhani yofanana ndi yomweyi yomwe ikupezeka ku mabuku a Marko ndi Luka ndi yomveka bwino zedi. Nkofunikira kudziwa kuti buku la Marko linalembedwera Ayuda ndipo iwo amamvetsetsa bwino lomwe miyambo yawo yokhudzana ndi kusudzulana komanso kukwatiranso. Yesu amawalankhula Ayuda molingana ndi kumvetsetsa kwawo. Pamene uthenga wabwino wa Marko unalembedwera Aroma ndipo wa Luka unalembedwera anthu amitundu ina, ndipo zonena zake ndi zomveka bwino pamene akukamba za chiphunzitso cha Khristu pa nkhanu ya kusudzulana ndi kukwatiranso. Mateyu 19:9 akulumikizitsa pamodzi mlaemba ena onse aja – kuti kusiya mkazi wako ndi kukakwatira wina pa chifukwa china chili chonse zili zotsutsana ndi chiphunzitso cha Khristu. ❖

“Ukwati ndi chinthu
chimene sichiyenera
kupasuka
mwachisawawa, ndipo
izi sizitengera zofuna
kapena ntchito za
anthu koma pa mfundo
zimene
zinakhazikitsidwa pa
chiyambi.”

—Matthew Henry



KODI MUKUDZIWA?

Mu Chipangano Chakale, pamakhala nyengo yayitali komanso yovomerekeza ndi lamulo imene mwamuna ndi mkazi a Chiyuda amene ali pa chitomero amayembekezera asanafike pokwatirana. Nthawi ya chitomero imeneyi inali yofunikira kwambiri ndipo ikusiyana ndi mwambo wa chinkhoswe umene umachitika kwawo kwa azungu. Ngati kwapezeka kuti mmodzi wa iwo wachita chigololo, chitomerocho chimathetsedwa monga mmene timachitira ndi kusudzulana. Chitomero, malinga ndi malamulo a Chiyuda, chinali ukwati umene.

Anthu awiri amene atomeranawo, ngakhale samakhalira limodzi monga banja, ndipo ukwati wao unali usanayambe, amadziwikabe ngati 'mwamuna' ndi 'mkazi' monga tikuonera pa nkhani ya Yosefe ndi Mariya mu Mateyu 1:18-19.



Mau a pa
Nyengo Yake

Kolezerani Moto

KUTI MUTIPEZE

The Gospel Truth
605 Bishops Ct.
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

Moto uziyakabe pa guwa la nsembe, wosazima. —Levitiko 6:13

Moto wa pa guwa pamene nsembe zimaperekedwa sumayenera kuzima. Moto sumangoyaka osayang'aniridwa, koma umayenera kusamaliridwa ndi kukolezedwa. Nkhuni zimayenera kusonkhezeredwa mosalekeza kuti motowo usazime.

Ukwatinso uli chimodzimodzi. Mulungu safuna kuti moto wa chikondi uzilare ndi kuzima. Chiyanjano chopatulika cha ukwati chiyenera kutetzedwa, ndipo chikolezedwe. Ma ukwati ambiri azilala chifukwa mwamuna ndi mkazi onse awiri sanatenge nthawi kudyetsera ubale wa banja lawo ndi chikondi komanso kudzipereka.



CHIYERO CHA KWA AMBUYE

Nkosavuta kwa anthu kukhala otanganidwa ndi ntchito komanso zosamalira za moyo uno. Pokhala atumiki, ndi kosavuta kukhala otanganidwa ndi ntchito ya Mulungu. Nkofunikira kuti atumiki akolezere moto wa banja lawo. Mdaniyo wayika misampha yambiri ndipo atumiki ambiri ataya njira yawo chifukwa sanasamalire zokolezera moto wao.

Banja lolimba limene moto umakolezedwa lidzapangitsa kuti ntchito ya mtumiki wa Mulungu ya uthenga wabwino ikhale yopindulitsa. Mtumiki sangathe KUSAPATULA nthawi kuti asalire moto wa panyumba. Akachita izi, zidzakhalira mdalitso kwa mkazi kapena mwamuna komanso ku ntchito ya Mulungu.

Patulani nthawi kuti mungokhala awiriwiri madzulo ena ake. Pitani kokayenda limodzi, sewerani limodzi... Zisiyeni kaye za ku ntchito kapena za bizinesi, kapena za kutchalichi, ndipo mungosamalira zakuti muli awiri basi.

KOLEZERANI MOTO! ♦

—mws